EXAMINATION NO.:________________

# THE MALAWI NATIONAL EXAMINATIONS BOARD

**2023 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION EXAMINATION**

# CHICHEWA

**Subject Number: M032/III**

**Thursday, 13 July**

**Time Allowed: 2 hours**
**8:00 – 10:00 am**

## PAPER III
(Malikisi 70)

**Malangizo:**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi awiri.**

2. Pepalali lili ndi magawo awiri: **A** ndi **B**.

3. Lembani **nambala yamayeso** pamwamba pa tsamba **lililonse la pepalali.**

4. Muchitebulo chili kumbaliku onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

5. Perekani pepalali kwa oyangánira mayeso nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani funso ngati mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| **Total** | | | |

© 2023 MANEB

## Gawo A (Malikisi 30)

### Nkhani za Mchezo ndi Zolembedwa

**Langizo: Yankhani mafunso onse m'gawoli pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

**1. Werengani ndakatulo ili m'munsimu ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

**N'CHIYANI CHAVUTA?**

Ndidalakwanji am'nanga
Kuti lero chikondi chathu chizikhala chonchi
Ngati wamapesi moto?
Gwero la msunamowu n'chiyani, Mbewe?

Dzana lija ndili kanjole kodya kokha
Mseko wopanda chiyambi chenicheni
Munkamasula nkhope yanu
Modolola mtimanga mtheradi.

Lero chasintha n'chiyani
Kuti muzindiyang'ana ndi maso aukali
Ngati womwa chiphe?
Langa khumbo n'kudzutsa chikondi chili mkafechi.

Ngakhale akataika saoleka
Mpatseniko mpata wowerenga
Lanu tsidya la maganizo
Kusiyana n'kuti tizingokhalira anawa.

Mafunso akupitirira/…

1. **(Continued)**

a. Kodi akuyankhula m'ndakatuloyi ndani?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

b. N'chiyani chomwe woyankhulidwa akuchita m'ndakatuloyi?

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

c. Perekani zipangizo **zitatu** ndi zitsanzo zake zimene mlakatuli wagwiritsa ntchito m'ndakatuloyi.

(i) Chipangizo: ______________________________

Chitsanzo: ______________________________

**(Malikisi 2)**

(ii) Chipangizo: ______________________________

Chitsanzo: ______________________________

**(Malikisi 2)**

(iii) Chipangizo: ______________________________

Chitsanzo: ______________________________

**(Malikisi 2)**

d. Fotokozani kamvekedwe ka woyankhula m'ndakatuloyi.

______________________________________________

**(Malikisi 2)**

e. Perekani matanthauzo a mawu awa:

(i) chizilale

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(ii) chiphe

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(iii) mkafechi

______________________________________________

**(Malikisi 1)**

Mafunso akupitirira/…

1. (Continued)

f. Perekani maphunziro **awiri** omwe akupezeka m'ndakatuloyi.

________________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

**2. Werengani nkhani ili m'munsimu mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.**

**MOYO WA GAZA**

Gaza adakhala moyo wovutika kwambiri kwa zaka zochuluka. Izi zidali tero chifukwa makolo ake onse adamusiya ali khanda lapsululu. Makolowo adachita ngozi ya galimoto akuchokera kuchipatala ndi mwanayo atangobadwa masiku awiri m'mbuyomo. Akubwerera kumudzi pagalimoto yawo, adaombedwa ndi galimoto ina yaikulu.

Gaza adaleredwa ndi agogo ake akuchikazi. Agogowa adali ndi mwayi wopeza mkaka wa mbuzi kapena wa ng'ombe. Izi zidali choncho chifukwa adali ndi ziweto zambiri ngati mchenga. Nthawi zonse ankaonetsetsa kuti akame mkaka wochuluka wokwanira kum'mwetsa mwana uja tsiku lonse. Iwo adali mzati wa Gaza.

Atafika paunyamata Gaza, azimu adamufulatiranso. Agogo ake aja adabzala chinangwa. Apa adadziwa kuti mvula ikakuona litsiro siikata. Gaza adalira ching'ang'adza tsiku lonse mfumuyo idakali m'nyumba kufikira kukaikidwa kunsabwera. Mwambo wamaliro utatha, agogo ake aamuna adamuyankhula mdzukulu wawo uja nati, "Mwana wanga, ugwire mtima. Dziwa kuti moto umapita komwe kwatsala tchire komanso kuti padziko lapansi munthu ali ndi masiku awiri: lakubadwa ndi lakufa. Iwe uyeneranso kudziwa kuti dzuwa likatuluka m'mawa timayembekeza kuti lilowa madzulo. Chinsinsi cha imfa chagona pamenepa. Ndiye tonthola ndipo ukhuzumuke. Nthawi zonse uziyang'ana kutsogolo ndi kulingalira kuti mawa libala chiyani."

Mafunso akupitirira/...

251

**2. (Continued)**

Gaza adali zyoli nthawi yonse agogo akewo ankamuyankhula. Kenaka iye adaweramuka ndi kuwalimbitsa mtima agogowo kuti kuyambira tsiku limenelo aziphika ndi kugwira ntchito zonse pakhomo paja. Iye adapitirira kukula mwathanzi. Nthawi zonse ankaonetsetsa kuti agogo ake akukhala mosangalala.

Tsiku lina madzulo, agogo aja adamuitana mdzukulu wawoyo. Iwo adati, "Mwana wanga, kufa n'kugona. Ndaganiza kuti mawa ndikakusonyeze malo athu kuti uzikhala ukudziwa moponda. Ndachita izi kuopa pam'mawa." Gaza adamvetsera ndi chidwi ngakhale kuti zamalo adalibe nazo ntchito nthawiyi.

Agogo aja adaitanitsa mikoko yogona isanu ndi mfumakazi zitatu kunyumba kwawo. Anthuwo atafika, agogo aja adati, "Ndaona kuti mwanayu akukula ndipo n'koyenera kuti tikamuonetse masala a kwawo poti chinziri chimanyang'wa patsala lake." Akuluakulu aja adavomerezana ndi agogowo. Onse adanyamuka ndi kukamusonyeza malo onse a agogo akewo. Gaza sankamvetsabe kufunika kwa mkumanowo.

Mwadzidzidzi, agogo aja adadwala chifuwa. Adakhala masiku asanu ali bwenzi lamphasa. Gaza adawawidwa mtima ndikudwala kwa agogo akewo. Tsiku lina Gaza adaitanidwa ndi agogo ake. Iwo adati, "Mwana wanga, ndikudziwa kuti sundimvetsa komabe tchera khutu. Mmene ndikuonera pano, ndatsala madzi amodzi. Nthawi ina iliyonse thambo ligwa, ndiye udzakumbuke mawu awa: sikadza kokha kaopa kulaula. Iwe bwenzi lako lidzikhala khasu chifukwa wamanja lende amakhala bwenzi la kadam'manja."

0128

Agogo aja ankayankhula ndi mdzukulu wawo uku akuyang'ana kumbali. Gaza adali ndi chisoni ndi mawu awa koma palibe chimene akadachita. Iye adakhala duu nthawi yonse agogo aja ankayankhula. Mwadzidzidzi, adangoona kuti asiya kuyankhula. Gaza adaitana agogo akewo koma kudali zii. Iye adachita kakasi.

Mafunso akupitirira/...

2. (Continued)

a. Tchulani komwe nkhaniyi ikuchitikira.

______________________________________________________ **(Malikisi 1)**

b. Lembani mphendero ya nkhaniyi.

______________________________________________________ **(Malikisi 1)**

c. Perekani mfundo **zitatu** zosonyeza kuti padali chikondi pakati pa Gaza ndi agogo ake aamuna.

(i) ______________________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) ______________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) ______________________________________________ **(Malikisi 1)**

d. Perekani chitsanzo **chimodzi** cha zipangizo zotsatirazi kuchokera m'nkhaniyi.

(i) chining'a______________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) chifanifani______________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) chiyerekezo______________________________ **(Malikisi 1)**

e. Perekani matanthauzo a nsinjiro za chiyankhulo izi:

(i) bzala chinangwa ______________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) manja lende ______________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) chita kakasi ______________________________ **(Malikisi 1)**

2. **(Continued)**

f. Lembani makhalidwe **awiri** omwe Gaza akuonetsa m'nkhaniyi.

(i) ______________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) ______________________________ **(Malikisi 1)**

g. Perekani maphunziro **awiri** omwe akupezeka m'nkhaniyi.

______________________________

______________________________

**(Malikisi 2)**

**Gawo B** (Malikisi 40)

**Langizo: Yankhani mafunso awiri okha m'gawoli m'ndime zofotokozedwa bwino.**

**NTHONDO (S J Nthala)**

3. a. Fotokozani zikhulupiriro **zinayi** zosiyanasiyana zomwe zikupezeka m'buku la Nthondo.

**(Malikisi 20)**

**KAPENA**

b. Tsimikizani popereka mfundo **zinayi** kuti Nthondo adaphunzira makhalidwe oipa kumphala komwe ankagona. **(Malikisi 20)**

Mafunso akupitirira/…

## CHAMDOTHE NDI ZISUDZO ZINA

**( S Likongwe, W Nkhoma)**

## CHAMDOTHE

**4.** a. Kuchokera m'chisudzochi, tsimikizani popereka mfundo **zinayi** kuti atengambali ena adali achikondi.

**(Malikisi 20)**

## KAPENA

## KHOSWE WAPADENGA

b. Kuchokera m'chisudzochi, tsimikizani popereka mfundo **zinayi** kuti khoswe wapadenga adaululitsa wapadzala.

**(Malikisi 20)**

251

0128

## MAFUNSO ATHERA PANO

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi awiri.**